EXAMINATION NO____________________________

# THE MKAIKA ZONAL MOCK EXAMINATION BOARD

2021 PRIMARY SCHOOL LEAVING CERTIFICATE MOCK EXAMINATION

# CHICHEWA

(Malikisi 100)

**Subject Number: P032**

**Thursday, 3 June** **Time allowed: 2h 15 mins**

**1:30 – 3:45Pm**

## Dzina lanu: ____________________________________________

## Dzina la sukulu yanu: ____________________________________

## Malangizo:

1. **Onetsetsani kuti pepala ili lili ndi masamba asanu ndi limodzi.**
2. Pepala ili lili ndi magawo anayi: **Gawo A, B, C ndi D.**
3. Lembani **dzina** lanu ndi **dzina la sukulu** yanu pamwamba pa tsamba lino.
4. Lembani nambala ya mayeso pamwamba pa tsamba lililonse.
5. Lembani chimangirizo kapena kalata mu **Gawo A** ndipo muyankhe mafunso onse mu **Gawo B, C** ndi **D.**
6. Lembani yankho la mu **Gawo A** pa pepala lapadera lomwe lili kumathero kwa mafunso a mu gawoli.
7. Yankhani mafunso a mu **Gawo B** ndi **C** m'mipata yomwe yaperekedwa pansi pa funso lililonse.
8. Yankhani mafunso a mu **Gawo D** pozuguliza lembo lokhoza pafunso lililonse.
9. Muchitebulo chili pamwambachi onetsani funso lililonse lomwe mwayankha pochonga mubokosi lomwe lilikutsogolo kwake
10. Perekani kwa okuyang'anirani kulemba mayeso **(Imvijireta)** pepala lonseli nthawi ikakwana.

| Funso | Chongani zomwe mwayankha | Muno musalembemo | |
|---|---|---|---|
| 1 | | | |
| 2 | | | |
| 3 | | | |
| 4 | | | |
| 5 | | | |
| 6 – 8 | | | |
| 9 – 15 | | | |
| 16 – 18 | | | |
| 19 – 20 | | | |
| 21 – 25 | | | |
| 26 – 30 | | | |
| 31 – 35 | | | |
| 36 – 39 | | | |
| 40 – 41 | | | |
| 42 – 43 | | | |
| 44 – 45 | | | |

# GAWO A: (Malikisi 30)

**1.** Lembani chimangirizo pa mutu uwu: "**Maphunziro"** Mwa zina tsatani izi polemba.

Ndime yoyamba

- Komwe maphunziro amapezeka.
- Ena mwa anthu ndi mabungwe omwe amathandiza pa nkhani ya maphunziro.

**Ndime yachiwiri**

- Zovuta zomwe zimapangitsa kuti maphunziro asamayende bwino.
- Njira zoyenera kutsatira kuti maphunziro aziyenda bwino.

**Ndime yachitatu**

- Kufunika kwa maphunziro

KAPENA

2. Lembani kalata kwa m'bale wanu yemwe amakhala kutali ndi inu yomufotokozera chitukuko chomwe chachitika kumudzi kwanu.
   Mwa zina tsatani izi polemba

**Ndime yoyamba**

- Fotokozani chitukuko chomwe chachitikacho.
- Tsiku, mwezi ndi chaka chomwe chitukukocho chidayamba.

**Ndime yachiwiri**

- Momwe chitukukocho chidayambira.
- Fotokozani zomwe inu mudachita pa chitukukocho.
- Fotokozani momwe chitukukocho chatukulira mudzi wanu.

**Ndime yachitatu**

- Zomwe mukuchita kuti chitukukocho chipitilire.
- Momwe mungalimbikitsire m'bale wanuyo kuti abwere kumudziko.

## GAWO B (MALIKISI 20)

**3. Werengani nkhani yotsatirayi mosamala kenako yankhani mafunso otsatirawo**

Ulimi umakhala wovuta ndi wofiiritsa maso ngati mlimi sadasamalire bwino munda wake. Kaufiti ndiye amafiritsa mbewu m'munda. Minda ya chimanga. Mapira, mchewere kungotchulapo zochepa, kaufiti ndimo amakondweramo ndipo mlimi akapanda kusamala sakolola kanthu chifukwa zimalephera kubereka.

Alimi ena kaufiti samudziwa, koma amakhala ndi timaluwa tofiira. Kaufiti akazulidwa amameranso ndipo amakonda kumera moyandikana ndi mbewu kuti azitha kukhaulitsa mbewuyo mosavuta. Achikumbi ambiri sathira manyowa a ziweto monga a ng'ombe m'munda mwawo ponena kuti kaufuti amadza ndi manyowa. Posadziwa kuti manyowa ndiomwe amabweretsa chonde m'nthaka.

Chuma chilim'nthaka makamaka mdziko lathu la Malawi chifukwa limapeza ndalama zambiri kuchokera ku mbewu zomwe alimiwa amalima. Komatu ntchito yolima imafuna kukhetsa thukuta, mkulu wa zaulimi mboma la Nkhotakota a Malikebu akuti ndowe zimathandiza kuti kaufiti asakhalemo m'munda ndipo ndibwino kuti alimi azithira manyowa.

Mukathira ndowe, kaufiti amatha dera limenero. Komanso alimi amayenera kubzala mbewu zina dera lomwe muli kaufiti monga mtedza, nyemba, zama, soya ndi fodya chifukwa kaufiti salimbana ndi mbewu zimenezi.

Kaufiti amamera ngati chonde chachepa m'dothi ndipo zikatero muthire manyowa dera limenelo. Kuchita zimenezi ndiko kumukhaulitsa kaufiti.

**Tsopano yankhani mafunso otsatirawa pamizere ili pansi pafunso lililonse**

a. N'chifukwa chiyani Kaufiti ndi woopsa zedi ku mbewu? (malikisi 2)

______________________________________________

b. Tchulani mbewu ziwiri zomwe zimadana ndi kaufiti (malikisi 2)

i. ____________________ ii. ____________________

c. Tingadziwe bwanji kuti uyu ndu Kaufiti? Perekani zizindikiro ziwiri (malikisi 2)

©2020 MKAZEB

i. ______________________________
ii. ______________________________

d. Perekani mawu ofanana m'matanthauzo ndi awa: (malikisi 2)
(i) Chonde: ______________________________
(ii) Ndowe: ______________________________

e. Fotokozani kufunika kuwiri kwa ndowe (malikisi 2)
i. ______________________________
ii. ______________________________

f. Tchulani njira ziwiri zomwe alimi angakhaulitsire kaufiti (malikisi 2)
i. ______________________________
ii. ______________________________

g. N'chifukwa chiyani m'minda ina mumamera kaufiti? (malikisi 2)

______________________________

h. Ndi mbewu ziwiri ziti zomwe sizikhudzidwa ndi kaufiti (malikisi 2)
i. _______________ ii. _______________

i. Kodi ndi mkuluwiko uti womwe ukutanthauza "**kuchita khama"** m'nkhaniyi? (malikisi 2)

______________________________

j. Tchulani dzina la mlangizi wa zaulimi mderan lanu (malikisi 2)

______________________________

k. Perekani mutu wa nkhani mwawerengayi (malikisi 2)

______________________________

## GAWO C (MALIKISI 10) Yankhani mafunso onse awiri mgawoli

4. Werengani kankhanika mosamala ndipo muyankhe mafunso otsatirawo.

***"Chete! Chete! Ndikatchula dzina la munthu, ngati alipo, azikalowa m'chipinda icho kuti akalandire katemera woyamba. Dziwani kuti, katemera wachiwiri apezeka pakatha masabata asanu ndi atatu".***

**Mafunso:**

a. (i) Ndi mtundu wanji wa malonje omwe aperekedwawa? (malikisi 1)

______________________________

(ii) Ndani akuyankhula nkankhanika?____________________ (malikisi 1)

(ii) Tchulani mtundu umodzi wa matenda omwe ali ndi katemera (malikisi 1)

______________________________

b. Perekani njira ziwiri zokha momwe mungasamalire sukulu yanu. (malikisi 2)
i. ______________________________
ii. ______________________________

**5. Kupanga ziganizo: Pangani ziganizo zomveka bwino ndi mawu awa:**

a. wamfupi: ______________________________ (malikisi 1)
b. du:______________________________ (malikisi 1)
c. luma:______________________________ ( malikisi )
d. iye:______________________________ ( malikisi 1)
e. mlendo: ______________________________ (malikisi 1)

**GAWO D ( MALIKISI 40)**

**©2020 MKAZEB**

Zungulizani lembo lokhoza (**A, B, C** kapena **D**) m'mafunso otsatirawa.

**Mafunso 6 mpaka 10**: Sankhani mitundu ya mawu amene ali ndi mzere kunsi kwawo m'ziganizo zotsatirazi:

6. Awo ngakuba
   A. Mneni C. Mlowam'malo
   B. Dzina D. Mfotokozi

7. Mbuzi zonse zili kwa a malume.
   A. Mperekezi C. m'neni
   B. Mvekero D. Mlumikizi

8. Hi! Mwana uja wagwa
   A. Mvekero C. Mfuwu
   B. Muonjezi D. Mneni

9. A Natembo ndi a Nthiko ali ndi galimoto.
   A. Mneni C. Mlumikizi
   B. Mperekzi D. mvekero

10. Anthuwa akusewera padiwa.
    A. Mfotokozi C. Mneni
    B. Muonjezi D. Dzina

**Mafunso 11 mpaka 15**: Sankhani magulu a mayina omwe ali m'munsimu.

11. Mwado
    A. I –, ZI C. Chi –, Zi
    B. Mu –, Mi D. Li –, Ma

12. Tombolombo
    A. U –, Ma C. Chi –, Zi
    B. Mu –, A D. Ka –, Ti

13. M'tchire
    A. Ku –, Pa –, Mu C. Ku –, ndi tsinde la mneni
    B. Mu –, Mi D. Chi –, Zi

14. Nsomba
    A. Chi –, Zi C. Ku –, Pa –, Mu
    B. Li -, Ma D. I –, Zi

15. Tulo
    A. Chi –, Zi C. Li –, Ma
    B. U –, Ma D. Mu –, Mi

**Mafunso 16 mpaka 18** Sankhani mitundu ya nthawi za aneni omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo m'ziganizo zotsatirazi.

16. Amisiri akumanga nyumba
    A. Yatsopano yathayi C. Yatsopano yopitirira
    B. Yatsopano D. Yatsopano yakawirikawiri

17. Anakhala akundinamiza kuti akubwera
    A. Yatsopano C. Yakele yathayi yopitirira
    B. Yakele D. Yatsopano yopitiriza

18. Dodolido amalima chimanga
    A. Yatsopano yakawirikawiri
    B. Yam'tsogolo
    C. Yakale
    D. Yatsopano yopitirira

**Mafunso 19 mpaka 20**: Sankhani mitundu ya alowam'malo omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo m'ziganizo zotsatirazi

19. Omwe agona asiyeni
    A. Woloza C. Wofunsa
    B. Wa umwini D. Wamgwirizano

20. Wayani akubwera apo?
    A. Wofunsa C. Woloza
    B. Waumwini D. Wochuluka

**Mafunso 21 mapka 22**: Sankhani mawu ofanana m'matanthauzo ndi omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo mziganizo zotsatirazi.

21. Iwo sakukhala pakhomo chifukwa cha chikwerete.
    A. Ngongole C. Chidani
    B. Chisembwere D. Chintchito

22. Yankho ndi Sankho akulimbirana Chivululu.
    A. Nthutumba C. Kapamba
    B. Matemba D. Chibodza

**Mafunso 23 mpaka 25**, Sankhani chaching'ono cha zinthu zomwe zaperekedwazi.

23. Ngo'mbe
    A. Mkota C. Mnthoni
    B. Msona D. Mphonda

24. Ndoda
    A. Mwana C. Muphwa
    B. Mnyamata D. Kamuna

25. Fodya
    A. Ndudu C. Mbande
    B. Njere D. M'mer

**Mafunso 26 mpaka 28**: Sankhani mitundu ya nthambi ya chiganizo yomwe yatsekedwa mzere kunsi kwake m'ziganizo zotsatirazi.

26. Zomwe ankafuna wazipeza.
    A. Yamuonjezi C. Yamfotokozi
    B. Yadzina D. Yoima payokha

27. Sindikusiya mpaka undigawire chigumu.
    A. Yadzina C. Yamuonjezi
    B. Yoima payokha D. Yamfotokozi

28. Wophunzira yemwe akufuna kupambana mayeso ayenera kulimbikira.

**©2020 MKAZEB**

A. Yadzina C. Yoima payokha
B. Yamfotokozi D. Yamuonjezi

**Mafunso 29 mpaka 30**: Sankhani chiganizo chomwe chili ndi zizindikiro zoyenera za m'kalembedwe.

29. A. Ogo! Madzi anga atayika.
    B. Ogo madzi anga atayika?
    C. Ogo? Madzi anga atayika.
    D. ogo madzi anga atayika!

30. A. Kodi wadwala lero
    B. Kodi, wadwala lero?
    C. Kodi wadwala lero?
    D. Kodi wadwala, lero?

**Mafunso 31 mpaka 34**. Sankhani matanthauzo a mikuluwiko yotsatirayi.

31. Mwana wamnzako ndi wako yemwe ukachenjera manja udya naye.
    A. Ana akamalerana okhaokha amakula bwino.
    B. Tizisamala ana athu kaye tisanasamale a ena
    C. Kuthandizana n'kwambino
    D. Udindo wolera ana ndi wa akulu
32. Padakafunda padajiwitsa galu
    A. Muvi umalasa okonda kugona.
    B. Kupeza mavuto chifukwa chakunyozera.
    C. Tizikonda kwambiri ana athu.
    D. Mavuto sayang'ana nkhope.

33. Fodya wako ndi uyu ali pa mphuno
    A. Tisamapemphe zinthu za anzathu.
    B. Zinthu za m'tsogolo zilibe ntchito.
    C. Tizidalira kwambiri za anthu ena.
    D. Tizidalira zinthu zomwe tili nazo.

34. Chikumbutsa nkhwangwa n'chisanu.
    A. Ntchito zina zimafuna kuthandizana.
    B. Zinthu zina zimafunika pa nthawi yake.
    C. Zinthu zina zimafunika nthawi zonse.
    D. Ntchito zimafunika kuzigwira utakonzeka.

**Mafunso 34 mpaka 35**: Sankhani ntchito ya "**ndi"** yomwe ali ndi mzere kunsi kwake m'ziganizo zotsatirazi.

35. Mtolo wanzimbe uli <u>ndi</u>.
    A. Mperekezi C. Mlumikizi
    B. Mvekero D. Mlowam'malo

36. Ophunzira ali <u>ndi</u> aphunzitsi awo.
    A. Mlowam'malo C. Mvekero
    B. Mperekezi D. Mlumikizi

37. <u>Ndi</u>dzalemba mayeso chaka cha mawa.
    A. Mlowam'malo C. Mvekero
    B. Mperekezi D. Mneni

**Mafunso 37 mpaka 49**: Sankhani matanthauzo a zilapi zotsatirazi:

38. Mbaleme yaikira paminga.
    A. Chisa C. Lilime
    B. Mphika D. Phala
39. Namng'omba wavundikira ana.
    A. Nyumba C. Denga
    B. Chisakasa D. Khonde

40. Kwathu kuli Mfumu zitatu, imodzi ikachoka, milandu sikambidwa.
    A. Mafuwa C. Dzuwa
    B. Misi D. Mphepo

**Mafunso 40 mpaka 43**: Sankhani mitundu ya alumikizi omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo m'ziganizo zotsatirazi.

41. A Nyoni anabwera <u>ndipo</u> apita.
    A. Wa mfotokozi C. Wa muonjezi
    B. Wa dzina D. Wa mneni

42. Aphunzitsi andipatsa kope <u>ndi</u> pensulo.
    A. Wa mneni C. Wa mfotokozi
    B. Wa dzina D. Wa muonjezi

43. Mtsikana waulemu <u>ndi</u> wanzeru amasangalatsa makolo.
    A. Wa mfotokozi C. Wa muonjezi
    B. Wa dzina D. Wa mneni

**Mafunso 43** mpaka **45**. Sankhani mitundu ya aonjezi omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo m'ziganizo zotsatirazi.

44. Iye amayenda <u>mothimbwidzika</u>
    A. Wa malo C. Wa nthawi.
    B. Wa mchitidwe D. wa chiwerengero

45. Ayanika zovala <u>pamwala.</u>
    A. Wa malo C. Wa mchitidwe
    B. Wa nthawi D. Wa chiwerengero

# MAFUNSO ATHERA APA

**©2020 MKAZEB**